Ukumbukirenso Mlengi wako masiku a unyamata wako, asanadze masiku oipa, kapena zisanayandikire zaka zimene udzati, Sindikondwera nazo;

MLALIKI 12:1



...pakuti ndingaliro ya mtima wa munthu ili yoipa kuyambira pa ubwana wake.... Genesis 8:21

Akamvera ndi kumtumikira, adzakhala ndi moyo wabwino, ndi zaka zawo m’zokondweretsa. Koma akapanda kumvera, adzawonongeka ndi lupanga, ndipo adzafa osadziwa. Koma onyenga mu mtima aunjika mkwiyo; Amafa ali ubwana, ndipo moyo wawo uli pakati pa zodetsedwa. Yobu 36:11-14

Pakuti Inu ndinu chiyembekezo changa, Ambuye Yehova: Inu ndinu chiyembekezo changa kuyambira ubwana wanga. Ndichirikizidwa ndi Inu kuyambira m’mimba; Salmo 71:5-6

Ndidzamuka mu mphamvu ya Ambuye Yehova; Mulungu, mwandiphunzitsa kuyambira ubwana wanga; Tsopano pamene ndikalamba ndi imvi, musandisiye Mulungu; kufikira nditawonetsa mphamvu yanu kwa mbadwo uno, ndi mphamvu yanu kwa onse ali nkudza. Salmo 71:16-18

Mnyamata adzayeretsa njira yace bwanji? pakusamalira monga mwa mawu anu. Salmo 119:9

Kondwera ndi unyamata wako, mnyamata iwe; ndipo mtima wako ukukondweretse masiku a unyamata wako, nuyende m’njira za mtima wako, ndi monga mwa maso ako; Chifukwa chake chotsa chisoni m’mtima mwako, ndi kuchotsa choipa m’thupi lako; Mlaliki 11:9-10

Simunadziwa kodi? simunamva kuti Mulungu wosatha, Yehova, Mlengi wa malekezero a dziko lapansi, safoka, kapena kutopa? nzeru zake sizisanthulika. Apatsa mphamvu olefuka; ndi kwa iwo amene alibe mphamvu awonjezera mphamvu. Ngakhale achichepere adzalefuka ndi kulema, ndi anyamata adzagwa ndithu; adzakwera mmwamba ndi mapiko ngati mphungu; adzathamanga koma osatopa; ndipo adzayenda, osakomoka.
Yesaya 40:28-31

Pomwepo anadza nato tiana kwa Iye, kuti Iye ayike manja ake pa ito, ndi kupemphera: ndipo wophunzirawo adawadzudzula. Koma Yesu anati, Lolani tiana, ndipo musawaletse adze kwa Ine: pakuti Ufumu wa Kumwamba uli wa totere. Ndipo Iye adasanjika manja pa iwo, nachokapo. Ndipo onani, wina anadza kwa Iye, nanena, Mphunzitsi Wabwino, chabwino nchiyani ndidzachita, kuti ndikhale nawo moyo wosatha? Ndipo anati kwa iye, Unditcha Ine wabwino bwanji? palibe wabwino koma mmodzi, ndiye Mulungu: koma ngati ufuna kulowa m'moyo, sunga malamulo. Iye adanena kwa iye, Iti? Yesu anati, Usaphe, Usacite cigololo, Usabe, Usacite umboni wonama, Lemekeza atate wako ndi amako, ndipo, Uzikonda mnzako monga udzikonda iwe mwini. Mnyamatayo ananena kwa Iye, Izi zonse ndinazisunga kuyambira pa ubwana wanga; Yesu anati kwa iye, Ngati ufuna kukhala wangwiro, pita, kagulitse zomwe uli nazo, nupatse aumphawi, ndipo udzakhala ndi chuma kumwamba; Koma m’nyamatayo pamene adamva chonenacho, adachoka ali wachisoni: pakuti adali nacho chuma chambiri. Mateyu 19:13-22

Ana inu, mverani akukubalani mwa Ambuye: pakuti ichi nchoyenera. Lemekeza atate wako ndi amako; (ndilo ndilo lamulo loyamba lokhala nalo lonjezano) kuti kukhale bwino ndi iwe, ndi kuti ukhale wa nthawi padziko lapansi. Aefeso 6:1-3

Munthu asapeputse ubwana wako; koma ukhale chitsanzo cha iwo akukhulupirira, m’mawu, m’mayendedwe, m’chikondi, m’chikhulupiriro, m’chiyero. 1 Timoteo 4:12

Thawanso zilakolako zaunyamata, koma tsata chilungamo, chikhulupiriro, chikondi, mtendere, pamodzi ndi iwo akuitana pa Ambuye ndi mtima woyera. 2 Timoteyo 2:22

Nzeru icokera ku mbali ina kufikira ku mbali ina ya mphamvu; Ndinamkonda, ndipo ndinamfuna kuyambira ubwana wanga, ndinafuna kumtenga mkazi wanga, ndipo ndinamkonda kukongola kwake. Nzeru ya Solomo 8:1-2

Mwana wanga, sonkhanitsa malangizo kuyambira ubwana wako, ndipo udzapeza nzeru mpaka ukalamba wako. Mlaliki 6:18

Peta mwana wako, ndipo adzakuopsa; Sewerani naye, ndipo adzakuvutitsani. Usaseke naye, kuti ungakhale ndi cisoni naye, kapena kukukuta mano pamapeto pake. Musamupatse ufulu pa ubwana wake, Ndipo musayang'anire pa kupusa kwace. Uweramitse khosi lake ali wamng’ono, ndi kum’menya m’nthiti pamene ali mwana, kuti angaumire, ndi kusamvera iwe, ndi kubweretsa chisoni mumtima mwako. Mlaliki 30:9-12